NYA_TTB_1101_SCRIPT

1 Yohane : 3:1-9

Mutu : Chikondi cha Atate kwa ana ake.

Moni upite kwa inuwokondedwa anzanga apaulendo m'dzina la Ambuye wathu Yesu kristu. Tiyeni lero Ambuye atitsogolere ndi mau apa Chibvumbulutso 5:9, amene akuti, "Ndipo ayimba nyimbo yatsopano, ndi kunena Mulungu muyenera kulandira bukulo, ndi kumasula zizindikiro zake; chifukwa mwaphedwa, ndipo mwagulira Mulungu ndi mwazi wanu anthu a mapfuko onse, ndi manenedwe onse, ndi mitundu yonse."

Mupologalamu yapita tinali kusanthula 1 Yohane 2:29-3:6, momwe timaunika za chikondi cha Atate pa ana ake. Ndipo lero pa 1 Yohane 3:1-9, tipitiliza kuona za chikondi cha Atate kwa ana ake.

1 Yohane 3

1. Taonani chikondicho Atate watipatsa kuti tichedwe ana a Mulungu; ndipo tiri ife otere. Mwa ichi dziko lapansi silizindikiraife, popeza silimzindikira Iye.

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti ife wokhulupirira sitiyenera kunena kuti tiyembekezakudzakhala ana a Mulungu ayi, koma kuti ndife ana a Mulungu kale. Tikunena kuti munthu aliyense amene atsimikiza mtima kuti anabadwa mwatsopano ayenera kutsimikiza kuti ndiye mwana wa Mulungu, kudzera mwa chikhulupiriro mwa Yesu Kristu. Kutsimikiza kuti wokhulupirira aliyense ayenera kukondwa ndi kusangalala ndi kuti nthawi yonse ayenera kuyamika Mulungu chifukwa chokhala mwana wa Mulungu. Mwanjira ina, ife wokhulupirira tiyenera kudzitamandira osati mwa ife tokha, koma kudzitamandira chifukwa cha M'busa wodabwitsa yemwe tiri naye. Ndiye pachifukwa chimenechi, Mtumwi Yohane akunenetsa kuti mwana wa Mulungu, ayenera kuonetsa khalidwe lomwe lifanana ndi Atate, kotero kuti sayenera kukhala wokaikira ayi. Ichi, ndichifukwa chake Yohane akunena kuti, ife lero lino ndife ana a Mulungu, osati tidzakhala ana a Mulungu ayi.

Tsono pamau akuti, "Taonani, chikondicho Atate watipatsa kuti titchedwe ana a Mulungu." Mtumwi Yohane akufuna kuonetsa za chikondi cha Mulungu chomwe ndi chodabwitsa, chosiyana ndi china chonse- chikondi chomwe ifetisanachionepo. Kutsimikizadi

kuti Mulungu atikondaife. Kodi ndi angati a ife amene abale athu akanatifera? Kapena tifunse kuti, kodi ndi anthu angati amene inu mukadafera?Apa, ndipamene mukhoza kuona kuti Mulungu akukondani inu, chifukwa ndiye anapereka Mwana wake kuti afe m'malo mwanu ndi mwa ine.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsa pano kuti chikondi ndicho chinthu chomwe ndichofunika kwambiri padziko lonse lapansi.Tikunena kuti chikondi ndicho chimene chimanga anthu kuti akhale pabanja, popeza mwamuna amagwa m'chikondi pa mkazi wake, komanso mkazi amagwa m'chikondi pa mwamuna wake.Ichi, ndichifukwa chake anthu awiriwa amalowapamalonjezano kuti adzakhala pamodzi kufikira imfa idzawalekanitse. Koma taonani chikondi cha Mulungu ndicho chiposa chikondi chapa banja, popeza palibe nthawi pomwe chikondi chake chimachoka pa ife. Ndiye Yohane pachifukwa chimenechi, akunenetsa kuti mwana wa Mulungu ayenera kuonetsadi kuti anabadwadi mumzimu pakumvera mau onse a Mulungu. Kunena kuti chikondi cha Mulungu ndichimene chiyenera kutikakamizaifekumumvera ndi kukhala m'moyo

wokonda Iye. Tere chikondi chotere ndichimene chathetsa nzeru Yohane kuti afike ponena kuti “Taonani chikondicho Atate watipatsa, kuti titchedwe ana a Mulungu.”

2. Okondedwa, tsopano tiri ana a Mulungu, ndipo sichinaoneke chimene tidzakhala. Tidziwa kuti pakuoneka Iye, tidzakhala ofanana ndi Iye, pakuti tidzamuona Iye monga ali.

Yohane akuyamba ndi mau achitsimikizo chakuti ife tiri ana a Mulungu pakali pano, osati mawa ayi. Koma dzikoli silingatimvetseife popeza linalepherakumzindikira Kristu. Ichi, ndichifukwa chakuti ndikosatheka kuzindikira zinthu zauzimu ndi mzimuwachibadwidwe.Tikunena kuti kuzindikira zauzimu kumadza ndi kudzoza komwe tinalandira patsiku lija tinabadwakwatsopano. Tere, ndiMzimuwa Mulungu wokha, womwe ungapereke chitsimikizo chakukhala mwana wa Mulungu, kotero kuti pamene Mzimuyuasoweka, inu mumakhala wokaika ngati munapulumutsidwa.

Tsono nkhani ikuti ife lero tiri ndi chitsimikizo chakuti ndife ana a Mulungu, koma sitikudziwa chomwe tidzakhala. Kutanthauza kuti sitikudziwa kuti maonekedwe athu adzakhala otani? Koma pali

chitsimikizo chakuti ife tidzazindikira maonekedwe athu panthawi yomwe Ambuye Yesu Kristu adzaonekapaulendo wake wachiwiri. Tikunena kuti pakali pano ife wokhulupirira sitinafikepamulingo womwe tidzakhala. Ichi, ndichimene Paulo anali kunena pa Afilipi 3:12, pamene adati, “Si kunena kuti ndinalandira kale, kapena kuti ndathakukonzekawamphumphu; koma ndilondetsa, ngatinsondikachigwire ichi chimene anandigwirira Yesu Kristu.” Ndipo pa verse 13, ndipamene akutsindika kunena kuti, “Abale, ine sindiwerengera ndekha kuti ndathakuchigwira: koma chinthu chimodzi ndichichita; poiwaladi za m’mbuyo, ndi kutambalitsirazamtsogolo.”

Tsono pakali pano inu ndi ine, tilibe chithunzi cha momwe tidzaonekera kotero kuti mwina timakhumudwapoona nkhope ndi matupi osiyana-siyana ya akristufe. Tere ndichifukwa chake Mulungu akunena kuti sitidziwa momwe tidzaonekera popeza ndiye yekha amene ali ndi chithunzi chimenechi mkati mwake. Ichi, ndichimene akunena kuti ife wokhulupirira tidzaoneka monga momwe Iye ali. Ndiye tiyenera kumvetsetsa kuti ifetidzaoneka ndi ulemerero wa Kristu, koma osafanana naye popeza Iye ndiye

Mulungu. Tikunena kuti chithunzi cha nkhope yanu ndi yanga zidzakhalabe monga momwe zionekera, koma tidzamvekedwa ulemerero wa Kristu kapena kunena kuti tidzafikapamlingo womwe Iye afuna. Ndifuna tizindikire kuti tikakafika Kumwamba inu ndi ine, tikatha kuzindikira abale ndi abwenzi.Ndikunena mau amene chifukwa Lazaro ndi mwini chuma onsewa atafaadazindikirana.

Tsono chinthu china chochititsa chidwi ndi chakuti Kumwambako, kukakhala kukonda munthu wina aliyense popeza tikakhala ndi matupi ofanana aulemererowa Kristu. Tere ndichifukwa chake Yohane akunenetsa kuti "Tidziwa kuti pakuoneka Iye, tidzakhala ofanana ndi Iye, pakuti tidzamuona Iye monga ali." Tsono mau awa, ndiwo amene ayenera kukhala chilimbikitso cha akristu onse lero lino, kuti tikaonana ndi Ambuye patsiku ilo.

3. Ndipo yense wakukhala nacho chiyembekezo ichi pa Iye, adziyeretsa yekha, monga Iyeyu ali Woyera.

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti ngati inu mukhulupirira kuti Ambuye Yesu akubwera ndipo kuti tsiku lina, inu mudzakhala ndi Iye, ichi chiyenera kukhala chinthu cholimbikitsa kukhala m'moyo

wachiyero.Tikunena kuti lero lino, sindife anthu oyeretsetsa, koma tsiku lina tidzakhala ofanana ndi Mbuye wathu Yesu Kristu.

Tsono masiku ano, anthu ambiri amanena kuti akuyembekeza tsiku lakubwerakwa Ambuye Yesu kachiwiri, pamene akukhala m'moyo wopanda chiyembekezo. Tikunena kuti sikungolankhula chabe, koma kukhala m'moyo woyenera ndiko.Kutanthauza kuti momwe mukukhalira masiku ano, ndicho chimene chidzaonetsa ngati inu mukuyembekezadi tsiku lakubwera Ambuye.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tikunenetsa kuti tsiku lina tidzakwanitsa kulowa mu Yerusalemu watsopano omwe adzakhala malo atsopano kumene Ambuye adzapukuta misozi yathu.Awa, ndimalo komwe kulibe chisoni, kapena kubvutika.Iyi, ndinthawi yomwe tidzaona zinthu zachilendo. Tamvani Yohane pa Chibvumbulutso 21:5, akunena kuti, "Ndipo Iye wakukhala pa mpando wachifumu anati, Taonani, ndichita zonse zikhale zatsopano." Kodi inu mukukhala m'moyo wachiyembekezo?

4. Yense wakuchita tchimo achitansokusayeruzika, ndipo tchimo ndilo kusayeruzika.

Pamene Yohane akunena kuti munthu aliyense wakuchita tchimo achitansokusayeruzika, akutanthauza kuti munthu wotere ndiye wophwanya lamulo.Kutsimikiza kuti kuchita tchimo ndiko kukhala wosalabadira lamulo.Tikunena kuti lero anthu aika moyo wawo pakuchita machimo ndipo sakulabadira lamulo la Mulungu.Ichi, ndichimene Yohane akunena kuti munthu wosalabadira lamulo, ndiye wokhala muuchimo.

Tikunena kuti Mulungu anaika malamulo khumi pa Eksodo 20, malamulo awa akanalipo, ndipo asanasinthe.Tikunena kuti malamulo awa anaikidwa ndi cholinga chakuti aletse munthu kuti asachite tchimo.Ndipo pamene inu muchita chinthu chomwe munaletsedwa, ndiye kuti mwachita tchimo. Mwanjira ina lamulo limationetsa kuti ndife wochimwa ndipo kuti tizizindikira chomwe Mulungu afuna. Lamulo linaikidwa osati ndi cholinga chakuti lipulumutse munthu, koma kuti ifetidzione tokha kuti ndife wochimwa ndipo kuti tifunikadi Mpulumutsi. Mwanjira ina, malamulo ndiwo galasiloonera, lomwe limaonetsa kuti nkhope yathu ndi yakuda ndi litsiro.

Tchimo ndilo kutsutsana ndi chifuniro cha Mulungu.Kutanthauza kuti munthu wochimwa ndiye amene atsutsana ndi chomwe Mulungu afuna kuti iye achite.Tsono tamvani kamtsikana kena ku Sunday sukulu kadanenapakuyankha funso lakuti tchimo m'chiyani?Iye adati ndikuchita chinthu chomwe munthu akonda. Ine, ndikuona kuti kamtsikanakamenekakadalondola ndithu chifukwa ganizo ili likugwirizana ndi zomwe Paulo adanena pa Aroma 8:5, pamene adati, "Pakuti iwo amene ali monga mwa thupi asamalira zinthu za thupi; koma iwo amene ali monga mwa Mzimu, asamalira zinthu za Mzimu." Kutanthauza kuti munthu amene akanali m'thupi amakonda, kulankhula ndi kuchitazinthu zathupi. Pamene munthu amene ali mumzimu, amakonda zinthu zauzimu. Yohane akunena kuti tchimo siligwirizana ndi moyo wakubadwa mwatsopano mwa Mulungu.

5. Ndipo mudziwa kuti Iyeyu anaonekera kudzachotsa machimo; ndipo mwa Iye mulibe tchimo.

Yohane mundime ino akunena kuti ndiambuye Yesu yekha amene angachotse tchimo popeza ndicho cholinga anadzera m'dziko lino. Ndiye pali zinthu ziwiri zofunika kwambiri kuti inu ndi ine,

tizidziwe. M'Uthenga Wabwino wa Yohane 1:29, tipeza mau akuti, "Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo la dziko lapansi!" Ndipo pa Yohane 3:16, tipeza mau akuti, "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wake Wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha." Mwa mau amenewa mukhoza kuona kuti Ambuye Yesu Kristu ndiyekhayo amene anasenza ndi kufa chifukwa cha machimo onse a dziko lapansi.Ndipo mu kalata iyi Yohane akuonetsa kuti Ambuye Yesu Kristu ndiyekhayo amene angachotse m'chitidwe wokhala muuchimo m'moyo mwa mkristu.Tsono pamene tiwerenga 1 Yohane 2:2, Yohane akuti, "Ndipo Iye ndiye chiombolo cha machimo athu; koma wosati athu okha, komanso a dziko lonse la pansi."Mundime iyi, muli pfundo ziwiri zofunika kwambiri.Poyamba tikuona ganizo lakuti Ambuye Yesu anafa imfa yopulumutsapoperekangongole ya machimo athu, komanso anafa kuti aombole wokhulupirira ku mphamvu ya tchimo pansi pano. Kutanthauza kuti mkristu ali ndi mphamvu yopewa tchimo pamoyo wake.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ili pano ikunena kuti mwa Kristu mulibe tchimo lina lililonse. Iyeyu anafa imfa ya chiombolo.Kunena kuti Yesu Kristu ndiye nsembe yoperekedwa chifukwa cha machimo athu.Iye ndiye Mwana Wankhosa wopanda banga la tchimo lina lililonse. Ichi, ndichifukwa chake ali ndi mphamvu yotipulumutsa ife ku chizolowezi chochita tchimo. Kunena kuti anatipatsa moyo watsopano wakuti tikhale wodalira Iye masiku onse a moyo wathu.Kodi inu, muli ndi chizolowezi chodalira Kristu muzinthu zonse?

6. Yense wakukhala mwa Iye sachimwa; yense wakuchimwasanamuona Iye, ndipo sanamdziwa Iye.

Pano tiyeni tiyambe ndi mau akuti Ambuye Yesu Kristu ndiye wopanda tchimo, amene mwachisomo anakhala tchimo m'malo mwathu ndi cholinga chakuti tiyanjanitsidwe ndi Mulungu. Iyeyu, kudzera mwa Mzimu, amakhala mwa wokhulupirira kotero kuti moyo wathu watsopano ndiwo moyo wake umene unaperekedwa kwa ife. Tsono nkhani ikuti ngati inu muli mwana wa Mulungu, moyo wanu watsopano sungathe kuyenda pamodzi ndi moyo wanu wakale. Kutsimikiza kuti wokhulupirira amene amakhala mwa

Kristu sachita komanso sakhala mu tchimo.Taonani chitsanzo chodziwika bwino paLuka 15:11-24, chankhani ya mwana wolowerera, tipeza kuti ndinkhumba yokha yomwe imakhala m'khola, osati mwana ayi. Tsono ndi mau amenewa, ine ndikukhulupirira kuti inu mwanena kale kuti, koma mwana analowa m'khola.Yankho likuti, ndizoonadi mwana adalowamkhola, koma kuti sadakhalemo. Kutanthauza kuti mwana wa Mulungu akhoza kuchimwa, koma sakhala mutchimolo. Ichi, ndichifukwa chakuti ndi mwana wa Mulungu, kotero kuti amafanana ndi Atate wake. Tikunena kuti Atate wake ndi woyera, kotero kuti mwana naye amafunika kukhala m'moyo wofanana ndi Atate.

Tsono pamau akuti, "Yense wakukhala mwa Iye sachimwa," akutanthauza kuti Mulungu amapereka mphamvu kwa ana ake kuti asachimwe. Koma pamene wokhulupirira abwererakumoyo wake wakale, ndipo ngati wokhulupirirayoangakhazikikemuuchimowo, ndiye kuti sanali mwana wa Mulungu. Tikunena kuti ngati inu mungakhalemutchimo ndi kumasangalala ndi kumaona kuti moyo

wanu ulibwino, ndiye kuti sindinu mwana wa Mulungu chifukwa ana a Mulungu ali ndi moyo wa Atate.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunena kuti ndichinthu cholimbikitsa komanso chofunika kwambiri kuti munthu wokhulupirira adziwe kulephera kwake.Munthu uyu, ndiye amene amasoweka mtendere ndipo sakhala wokondwa pamene wagwapatchimo. Tsono Uthenga kwa inu, amene mukusoweka mtendere chifukwa cha tchimo, ndiwakuti Mulungu lero lino ali wokonzeka kukumasulanikusinga za tchimo limeneli. Tikunena kuti lero muyenera kumpempha Ambuye kuti akubwezeretseni kumalo a mtendere ndi chimwemwe. Kutanthauza kuti ngati inu muli mwana wa Mulungu, simungakhutitsidwe kukhala mutchimo. Tsono Yohane akuti ndiMulungu yekha amene angakumasuleni inu popeza ndinu mwana wake.

7. Tiana, munthu asasokeretse inu; iye wakuchita cholungamaali wolungama, monga Iyeyu ali wolungama.

Tsono pamene Yohane akunena kuti “munthu asasokeretse inu; iye wakuchita cholungamaali wolungama,” alikunena kuti kukhala mwa Yesu Kristu ndi kofunika kwambiri ndipo palibe wina

angakwatule inu m’dzanja la Ambuye, koma kukhala mwa Ambuye m’chiyanjano ndi mkutumikira ndiko kumene kungapangitse inu kukhala wolungama. Tikunena kuti inu mukhoza kukhala pakati pa anthu woipa, koma pamene muitanira pa Ambuye nthawi yonse, Mulungu ali wokonzeka kukumasulanikumphamvu ya tchimo.

8. Iye wochita tchimo ali wochokera mwa m’dierekezi chifukwa m’dierekezi anachimwa kuyambira pachiyambi. Kukachita ichi Mwana wa Mulungu adaonekera ndiko kuti akaononge ntchito za mdierekezi.
9. M’menemo aoneka ana a Mulungu, ndi ana a mdierekezi: yense wosachita chilungamo siali wochokera mwa Mulungu; ndi iye wosakonda m'bale wake.

Nkhani ili mundime izi ikuti mdierekezi anakonza kuti aononge ntchito za Mulungu m’dziko lapansi. Pamene Mwana wa Mulungu ndiye analowa pankhondoyauzimu kutsutsana naye m’dierekezi. Mwana wa Mulungu anadza m’dziko lapansi m’thupi kuti akakhozekugonjetsa mdierekezi ndi kuononga ntchito zake zonse. Tere ntchito za mdierekezi zikuononge ka pang’ono ndi pang’ano kufikira zidzatheratu zonse patsiku lilimkudza. Pachifukwa

chimenechi, ifewokhulupirira sitiyenera kulowa ndi kukhala m'zinthu zimene Ambuye anadza kudzaononga.

Ndiye tiyeni titsirize ndi mau akuti, chipembedzo si luso kapena kuchita mwaluntha ayi, koma chitanthauza kukhala m'moyo watsopano.Zotsatira za kubadwa mwatsopano ndi kukhala m'moyo wosachita tchimo.Koma ngati tikugwapatchimo, ndiudindo wathu kulapa tchimolo, Mulungu aliwokonzekakutikhululukira machimo onse.Kutsimikiza mau a Yohane akuti wokhulupirira sangachite tchimo. Mwanjira ina akunena kuti wokhulupirira ngati angagwem'tchimo, koma sangakhazikike m'menemo. Kodi inu mumamva bwanji pamene mukugwapatchimo?

Kwalerotilekeza pano ndipo timasanthula 1 Yohane 3:1-9, tipitiliza kuona za chikondi cha Atate kwa ana ake.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!